Thangato la alimi ndi kuwonongeka kwa ndalama za dziko

duducoelho.com

Ndondomeko ya thangato ku alimi lithandizidwa ndi ma boma a maiko kuti lithandize alimi ang'ono-ang'ono. Koma zitupa zotolelapo za ulimi ndi fataleza nthawi zina **zimabedwa** ndipo nthawi zambiri **zipatsidwa** ku alimi omwe safunika kulandila thandizo limeneli monga azamalonda ndi alimi akulu-akulu.

Pali **chilungamo chochepekera** pa malonda a mbeu ndi fataleza, cinthu chomwe cipangitsa kukhala cobvuta kudziwa unyinji wa ndalama za boma zomwe ma kampani a fataleza ndi mbeu amalandila. Palibe njira zoyanganila malonda amenewa ndipo ngati zilipo zilibe mphamvu. Ndicosadziwika unyinji wa fataleza ndi mbeu zomwe zimasowa.

Mu maiko ambiri aku m'mwela kwa Africa, zaulimi zomwe zipekekedwa kupyolera mu ndondomeko ya thangato ya alimi zimabedwa zikalibe kugawidwa ku alimi (diversion), ndipo alimi amagwiritsa nchito zitupa kutenga ndalama m'malo mwa zaulimi kapenanso ugulitsa zaulimi ku ena (leakage).

- **Tanzania** – Fataleza yofika 60% inabedwa ikalibe kugawidwa ku alimi
- **Zambia** – Zaulimi zofika pa 35% zinabedwa kapena ugulitsidwa ku anthu ena kapenanso alimi anatenga ndalama m'malo mwa zaulimi
- **Malawi** – Zaulimi zofika pa 33% zinabedwa kapena ugulitsidwa
- **South Africa** – Zaulimi zochuluka zinabedwa ndi kugulitsidwa ku alimi m'dziko kapena kugulitsidwa kunja kwa dziko mwa katangale

african centre for biodiversity

www.acbio.org.za info@acbio.org.za Tel +27 (0)11 486 1156